Ngati ndingakufunseni tikumwa khofi, ‘’Kodi ulendo wanu wa uzimu unayamba kwenikweni liti mmoyo wanu ngati wamkulu’’ kodi mungandiuze chiyani? Munali kuti? Kodi zochitika zake zinakhala bwanji?

Kwa ine, unali usiku umene ndinamaliza maphunziro anga a secondary school. Nditatha kucheza ndi anzanga ena kumphwando ndinazindikira kuti ndine munthu wolimbikira ntchito. Ndinali wopambana kumaphunziro. Loto langa lokapitiliza maphunziro a masewera a mpira onjanjitsa anali mmanja mwanga. Ndinapezeka ndikusewera maligi onse a baseball. Ndinali pa chibwenzi ndi mtsikana wooneka bwino. Ndinakhala ndekha pansi, osungulumwa, ndimasinkha mudziko muno ndikukhaliranji. Njira yanga yakuti ‘’kupambana kuzakupangitsani kukhala wokondwa’’ sikunaphule kanthu.

Ndikukumbukira usiku umenewo nditakhala pa kama wanga, ndikuyang’ana panja pa zenera chipinda changa chogona. Unali usiku umene kunali nyenyezi zambiri, ndikukumbukira. Ndipo ndinayamba kufunsa mafunso enieni amene anthu akulu amafunsa. Chifukwa chiyani ndili pano? Kodi Mulungu alipo? Kodi cholinga changa m’moyo ndi chiyani? Kodi pali china chokhudza moyo kuposera kuyala zolinga ndi kuzikwaniritsa izo? Ndipo usiku umenewo, ngakhale kuti ndinali ndi mapephero a ku chibwana, ‘’Nditulutseni muukonde ‘’ ndi ‘’chonde ndithandizeni ndi zina Zotero.’’ Usiku umenewo ndikuganiza kuti ndinapephera pemphero loyamba mmoyo wanga ndili wamkulu. Ndipo ndikukumbukira ndikuyang’ana nyenyezi ndi kunena, ‘’Mulungu ngati mulipodi, mudziulule Nokha kwa ine mu njira imene ndingamvetse.” Ndipo kenako ndinazindikira kuti aliyense amafuna china chake, ndikukumbukira ndikupemphera,’’Mulungu, kodi chimene mukufuna kwa ine ndi chiyani? Ngati mulipodi, kodi chenicheni chimene mukufuna kwa ine ndi chiyani? “

Ndipo ichi chiikhala funso limene tifunse ndi kuyakha lero pa ulendo wathu wopita ku uzimu weniweni. **Kodi timapereka bwanji kwa Mulungu chimene iye amafuna kwambiri?** Tiyenda muulendo umenewu ndipo utitengera ife pa malo amene achiganizo chofunikira kwambiri.

Pamene mwafunsa mafunso akulu pa moyo, amabwereranso kwa inu munjira imene muli ziganizo zazikulu, ziganizo zokhudza tsogolo lanu ndi zofunikira kwambiri kuposera ntchito ndi ndalama ndi tsatanetsatane wa zonse.

Choncho ndikufuna kukudziwitsani za bukhu limene ndinawerenga. Linalembedwa ndi mphunzitsi wa ku Yale Law lotchedwa ‘’Chiwopsezo, chifukwa ndi dongosolo lopanga chiganizo.” Ndi ndandanda wa nkhani zochitika zimene zili ngati nkhani zofunika kulingalira.

Amagwiritsa ntchito ku Harvard Business school. Amawerenga nkhani zofunika kulingalira, amakhala mmagulu ang’onoang’ono ndi kukambirana. ‘’Chabwino, Kodi ziwopsezo zinali zitizo mmene popanga chiganizochi ndi zifukwa ziti zimene anthu anapangira chiganizo ichi, ndipo inu mungachite chiyani? Ndiye amakhala ngati achisenda, ndikupereka nkhani yofunukira kulingalira

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

ndi kulola magulu akambirane pang'ono kenako amawapatsa nkhani yonse. Cholinga chawo ndikuwaphunzitsa kupanga ziganizo zaluso ndi zanzeru.

Ndili ndi nkhani zofunika kuganizira zingapo pano, chifukwa zitithandiza kukamba za chiganizo chofunikira kwambiri ndipo nkhani zimenezi zidzatipatsa ife chizindikiritso chachikulu chokhudza kupanga ziganizo.

Ndi zachidule, koma ndizosangalatsa choncho nkhani yofunika kulingalira nambala 1. Injiniya wazaka 32 wotchedwa John amakonda kupita ku msika wa zachuma wa zinthu zogulitsa zakale wa katundu wa mnyumba ndi zinthu zina zaphindu. Kumapeto kwa sabata lina lake, amapita ku msika wa zachuma wa kummwera kwa United States. Katundu yense mnyumba mmenemu amagulitsidwa pa mtengo umodzi. Alendo anali olandilidwa kupikisana, ndipo John anadziwa kuti wopikisana wopambana adzagula pafupifupi $95000.

Nyumbayo ndi yowonongeka, mwina mwake inamangidwa munthawi ya nkhondo ya pa chiweniweni mu zaka za ma 1800. John wodzimva yekha ukatakwe ndi katswiri wa mbiri yakale, anazindikira mulu wa umene anasonyeza kuti zinagwiritsidwa ntchito nthawi imeneyo. Ndiye kenako analowa pansi panyumba – pogwiritsa tochi yayi ng'ono, anapeza tebulo lotembenuza, ndipo poyang'anitsitsa desikiyo, anapeza kabati yongoyerekeza. Ndipo mukabati muli chikwama chachikopa chimene chili ndi ndalama zachitsulo zagolidi zosowa, zimene zinali za golide weniweni, zojambulidwa ndi Confederate Army mnthawi ya nkhondo ya pachiweniweni. Anakhulupirira kuti zikhoza kukhala za ma doll mamiliyoni ochuluka
.
John anafunsidwa apange chiganizo. Achite chiyani? Anasunga $10000 ku banki. Ngati angagulitse galimoto yake ndi nyumba yake ndi chili chonse chimene ali nacho, akukhulupirira akhoza kupeza $95000 ndi kupambana pa mpikisano wogula. Kodi achite chiyani? Ophunzira aku Harvard Business school, aku MIT ndi sukulu zina za ukachenjede anakambirana izi. Choncho powona phindu la pamaso, mungachite chiyani? Ganizirani za izi.

Nkhani yofunika kulingalira nambala 2. Sheilla mphunzitsi wa luso lojambula wa zaka za mmaso ku Community College amayenda mu Europe mu nthawi ya chirimwe. Anali atangoyamba kusonkhetsa zojambula zosiyanasiyana ndi ndalama za malipiro ake ochepa. Ndipo ali mmudzi wina waung'ono kummwera kwa France, ali munjira sheilla anapita ku malonda a obetchera kumene anthu a mmudzimo anagulitsa zojambula za banja zongoperekedwa mwachithandizo kuti zigulitsidwe zithandizire ku ndalama zomangira sukulu yofunikira kwambiri.

Chojambula chimodzi chinaposa zonse, ndipo chinanedwa kuti ndi chosowa kwambiri, koma chinali chokwera mtengo wa ntchito za Picasso. Chinanenedwa kuti sichinali chenicheni chifukwa chidindo chake pansi pake chinali chosiyana ndi ntchito zake zina zonse. Komabe Sheilla analemba Nkhani yake ya maphunziro a Masters Ku College inali ya Picasso ndipo anadziwa kuti zaka zake zoyamba kujambula, sanasayinire dzina lake koma malembo ake oyamba a dzina lake.

Anayang'ana ndi kuwerenga chojambulacho mosamala ndi kutsimikiza kuti alidi pakati pa chithunzi chamtengo wapatali kwambiri. Panali chikhulupiriro chakuti panali zithunzi ziwiri kapena zitatu

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

zokha zopezeka mu zithunzi za padziko lonse lapansi. Ngati ichi chinali choncho, ndiye kuti Sheilla anayima pamaso pa chinthu chimene chinali cha phindu la ndalama zambiri.

Mtengo wa $2500 umene unaperekedwa zinali ngati nthabwala zenizeni polingalira phindu lake, komanso zinali nthabwala zenizeni poyerekezera ndi malipiro ake a pa mwezi. Chimene Sheilla akanachita ndi kugulitsa galimoto yake ya Volkswagon kugulitsa zojambula zonse zimene anasonkhanitsa mmbuyomo ndikutenga ndalama zake zonse zimene anasungitsa ku banki zokwana $600. Kodi Sheilla akadachita chiyani? Kodi mungamuuze chiyani?

Muzindikira kuti mu zolem bamwanu ndinaphatikiza mafunso akuti mulingalire, ndipo mukakumana ndi zokhala ngati izi, mmafunsa,''Chabwino, kodi ziwopsezo ndi ziti?" Chiwopsezo ndi chakuti ngati ndalama zachitsulo ndi zabodza ndiye kuti John wachita kale zimenezo, adzaluza chilichonse, ndipo chiwopsezo kwa Sheilla ndi chakuti, ngati sicha Picasso, adzaluza chilichonse. Kenako mu nkhani yofunika kulingalira. pa tsamba lachiwiri limene mphunzitsi walitulutsa-likunena kuti ndalama zachitsulo ndi zenizeni. Ndipo ndi mtengo wake ndi $30 mpaka $40 miliyoni cha Picasso chinali chenicheni ndipo mtengo wake unali $100 miliyoni. Choncho mphotho zake zinali zapamwamba, makamaka ngati zinali zowona. Koma mtengo wake ndi chiwopsezo zinali zowopsa kwambiri, koma ngati sichoncho. Ndi nkhani imeneyo, Kodi mukanachita chiyani ndi chifukwa chake?

Tsopano ndikufuna ndikupatseni mfundo zitatu kuchokera ku nkhani zofunikira kulingalirazi. Pano pali chimene inu ndi ine tilunjike. Muchiganizo chilichonse chachikulu- chofunikira, chiganizo chositha moyo- chinthu choyambirira chimene musowekera ndi - mulemba mawu awa – **Choonadi.**

Nkhani ili pano ndi choonadi cha zimene apeza. Ngati ndalama za chitsulo zili zovomerezeka, ngati zili zoona, ngati chithunzi chinajambulidwa ndi Picasso, ngati chili choona… Kwa inu pamene mukuyesetsa kuganizila chimene mungachite ndi moyo wanu ndi maubale amene muli, mukusowekera choyamba ndi chofunikira kwambiri ndikufunsa, "Kodi choona ndi chiti?"

Chachiwiri, lembani mawu akuti **chidziwitso** pansi pa zinthu zanu zoyang'anitsitsa. Onani, Sheilla anali ndi chidziwitso chimene anthu ena analibe. Anali atagwira ntchito ina, anali ataphunzira. Anali wokonzeka kugwiritsa ntchito mwayi wopezeka kugwiritsa munthawi imeneyo chifukwa anadziwa zinthu zimene anthu ena sanadziwe. John analinso choncho. Anali katakwe wa makina a computer. Katswiri wa mbiri yakale. Pamene anawona mfuti anawona nyumba, zinthu zonse izo zinamupatsa chidziwitso chamkati chokhudza chenicheni chimene akuchiyang'ana.
Ndipo kenako tikatha choonadi ndi chidziwitso chomalizira chimene musowekera… lembani mawu akuti **chikhulupiriro.**

Izi ndi mfungulo zitatu zopangira ziganizo zazikulu kwambiri. Kodi **choona** ndi chiyani? Kodi muli ndi **chidziwitso** chamkati? Ndipo kenako **chikhulupiriro** ndi chilimbikitso cholizira mfuti kupanga kuti chitheke.

Ndi chinthu china kuti John anene kuti. "Hee, ndikukhulupirira ichi. Ichi ndi choona ndachiyesa." Ndipo kenako mungathe kumva John akubwera kukayankhulana ndi mkazi wake? "Hee

wokondedwa, tidzatapa ndalama zonse zimene zili ku banki, tigulitsa nyumba ,tigulitsa galimoto, chili chonse chimene tili nacho, chifukwa ndapeza ndalama izi zachitsulo ndipo… Ndikutha kuwona iye akugwedeza mutu wake.

Ndipo ngakhale kuti ali ndi chitsimikizo chenicheni - chifukwa chakuti ndawona izi zikuchitika kwambiri - mukudziwa pali zinthu zimene mumakhala ndi chitsimikizo chake chimene mukukhulupirira kuti ndi choona ndipo mfundo zanu zikukuuzani kuti ndi choona. Nthawi zina, ngakhale Baibulo limakuzani kuti ndi choona. Pa nthawi zina, kafukufuku ndi mbiri yakale zimanena kuti ndi choona. Koma pomwe mukuyang'ana kulemera kwa chiwopsezo chake, pali gulu lalikulu la anthu amene alibiretu chikhulupiriro kapena mphamvu zowombera mfuti ndi kuchitapo kanthu pa zimene akukhulupiriradi kuti ndi choona. Ndiye choncho sapanga chiganizo kapena kusapanga chiganizo chimene chili chiganizo pachokha.

Nkhani zofunikira kulingalira ziwiri izi zikundikumbutsa ine za nkhani yofunikira kulingalira ya Yesu imene anaphunzitsa ife yokhudza chiwopsezo, chifukwa ndi ndondomeko yopanga chiganizo. Pamene Yesu akuphunzitsa ichi – chikupezeka mu Mateyu 13:44-45 - pa nthawi iyi, kutchuka kwake kumakula … amaonedwa kuti ndi mfumu ya dziko lonse lapansi, Mpulumutsi. Ndipo akunena kuti, "Ndine mfumu wa ufumu ndi chimene ufumu wonse uli, uli ndi maufulu ndi mphamvu ndi ulamuliro zimene munthu wina angalamulire."

Ndipo amaphunzitsa njira yatsopano ya moyo yosiyaniranatu kuchokera pa nthawi yachipembedzo imeneyo. Anali wokonda, ndipo anali okoma mtima ndipo anali oyera ndipo anali wathunthu. Ndipo kuli konse kumene anapita, kunali mwina chisokonezo kapena chitsitsimutso. Ndipo panali china chimene chinali chochititsa chidwi ndi champhamvu. Anachita zinthu zimene palibe wina aliyense anapangapo. Anaukitsa anthu akufa ndipo anayankhula za Mulungu ndipo anavumbulutsa za Atate.

Ndipo anthu anayamba kumalondola iye. Ndipo pamene anayamba kumulondola iye. Zinawakakamiza iwo kupanga ziganizo zazikulu, ziganizo zazikulu za mmene ankaganizira poyamba; ziganizo zazikulu za nthawi yawo kapena ndalama zawo kapena tsogolo lawo.

Choncho Iye amawapatsa mafanizo awiri kapena zithunzi ziwiri - miyambi. Anachita kuwapanga. Akuti, "Ufumu wa kumwamba…" Mmawu ena, "kutsatira Ine ndi mmene moyo umayendera ndi Ine monga ngati Mfumu ya moyo wanu kuli monga chuma chobisika mmunda chimene munthu wachipeza, kenako ndikuchibisanso, kenako kuchokera kwa chimwemwe pa icho, amapita ndi kukagulitsa zonse zimene ali nazo ndipo ndikugula mundawo."

Tsopano, umenewo ndi uthenga koma muli zazikulu mmenemo. Mwina mwake chopezekapezeka muchiphunzitso chachiyuda – mofanananirapo - adzakupatsani choonadi ndi kuonetsetsa kuti mumvetsetse, kapena kukupatsani chenicheni cha choonadi chomwecho ndi mwachithunzi china.

Onani ndime 45. "Ndipo ufumu wa kumwamba uli wofanana ndi munthu wa malonda, wakufuna ngale zabwino" - wa mtengo waphindu wokongola; choposera mtengo wapatali phindu lake ndiye maganizo ake – "anapita ndi kugulitsa ngale zonse zimene anali nazo ndi kuwugula iwo."

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

Ngati muli ndi cholembera,chitengeni. Tiyeni tonse pa ndime 44. Ndikufuna kuti inuyo muwone china chake. Mulembe mzere pansi pa mawu awiri “chuma chobisika”. Ndiye kenako, mawu awiri “chuma chobisika”. Ndiye kenako, mawu awiri “munthu “kupeza”. Ndiye kenako mawu awiri “bisa” “nso”. Ndiye kenako, mawu awiri “kuchokera” “chimwemwe”. Ndiye kenako “kugulitsa” “zonse”. Ndiye kenako mawu akuti “kugula mundawo”.

Ndipo ngati tikusanthula Baibulo pamodzi ndinganene kuti pali zinthu zinayi zoyang’anitsitsa zimene tingapange zimene zili zosavuta kwambiri koma zovumbulutsa chimene Yesu akunena. Munthu, choyamba, akupeza chuma, Munthu, atapeza chuma, chachiwiri, anawona kuti ndi cha mtengo wanji. Akuchibisanso. Chachitatu, anachita monga mwakumva kwamaganizo kusangalatsidwa mwamtheradi ndi wachimwemwe chimene chinabwera chifukwa cha ndalamazi. Ndiye kenako, chachinayi, pofuna kupeza mundawo, akugulitsa chilichonse chomwe ali nacho kotero kuti mundawo ukhale wake, adzapeza chuma chimene chili mkati mwake.

Tsopano, pali chinthu chimene muyenera muchimvetse. Yesu sakukamba za ndalama ndi chuma. Akupereka mfundo yofunikira kwambiri ya uzimu ndi lamulo lokhudza kupanga chiganizo. Ndipo chimene akunena ndi ichi, pali zinthu zina zimene tingawone ndipo pali zinthu zina zimene sitingawone. “Ndi Ufumu wa Mulungu ndi kutsatira Ine ndi zofana…” Akupereka zitsanzo izi.

Ndipo izi zinali zomveka mmasiku awo chifukwa izi zinali zochitikadi mmasiku awo. Analibe 401K’s. Ndipo mumatha kutenga chuma chanu ndipo mumatha kuchibisa ndi kuchikumbira pa malo penapake mmunda mwako. Ndipo cholinga chinali chakuti mudzawauza abale anu, ana anu amuna kapena akazi- pamene chili. Koma nthawi zina, anthu samakonzekera, ndipo amafa asanawuze aliyense. Chimatha kukhala mmunda kwa mibado iwiri kapena itatu kapena inayi.

Ndipo anthu anaganiza kuti nkhaniyi ndiyoyimbika. Ndipo akunena kuti, “Pano pali munthu amene ali kumunda. Mwina mwake akuyenda ndi ndodo, ndipo akumva china chake, ndipo akuchitsegula, ndipo pali kabati yaying’ono, ndipo muli ndalama. Ndipo akutsekanso ndi ndiwokondwera kwambiri ndi chimene wapeza. Choncho mosasamala, mongotaya, akugulitsa chilichonse chimene ali nacho chimene chilibe phindu kwenikweni kuti apeze chinachake chimene chili chaphindu kwambiri.”

Chomwechonse ndi chithunzi cha ngale.

Pano pali ndemanga yake, Yesu akunena kuti pomwe inu mwamvetsa kuti Iye ndi ndani, ndi mmene moyo umayendera ndiye panopa chimene chili choyenera tsopano mpaka muyaya- ndi kupeza chuma chimene ndi kukhala ndi ubale ndi Iye – ndi dongosolo limene ali nalo pa inu la padziko lino lapansi- mungathe- ndi kutaya mosasamala ndi chimwemwe- kusiya chili chonse kuti muchipeze.

Tayikani mnjira ina, ndemanga Yake ndi: kudzipereka ndi njira imene madalitso akulu kwambiri a Mulungu amakhuthukira. Kodi mwazindikira chimenecho? Ndikutanthauza, kudzipereka kwathunthu. Anagulitsa chili chonse chimene anali nacho. Cholinga? Chimwemwe.

Pamwamba pa mawu mu zolemba zathu, pomwe pakunena kudzipereka kwathunthu, mungathe kulembapo mawu akuti “kugonjera” ndi kujambula bokosi mozungulira? **Kugonjera <u>kudzipereka kwathunthu.</u>** Ndi zonse kapena popanda ndi cholinga chopeza malo ndi chuma chili mkatimo.

Tsopano, onani mmene Webster akutitanthauzira kudzipereka kwathunthu, chifukwa nthawi zina mawu amenewo amatanthauza zina mawu amenewo amatanthauza zinthu zina zosiyana kwa anthu ena. Akunena kuti, “Ndi kuyika mondandalitsa zolinga, zipangizo, zofunikira kwambiri ndi zokhumba za munthu kukwaniritsa mayitanidwe a padera, kukwaniritsa ntchito yapadera, kapena kutsatira munthu wapadera. Mmawu kapena kutsatira munthu wapadera.” Mmawu a “Texas Hold Em” kusewera masewero a khadi “imene mulimo wense”.

Kudzipereka kwathunthu. Kugonjera. Izi ndi zotsutsana kwambiri. Yesu ndi mphunzitsi uyu odabwitsa oyitanira anthu ku moyo ndipo akunena kuti maphindu ake atembenuzika mudziko limene mukukhalamo. Ndipo njira yopindulira ndi kupereka- ndi njira ya moyo ndi kufa. Ndipo akuti, “Ndili ndi dongosolo, ndi potsata Ine ndi pamene pali chuma chimene chili chosasimbika. Ndi chosasimbika tsopano. Chidzakusinthani. Chidzasintha ubale muyaya. Chili ndi cholunjika ndi cholinga ndi mayakho ku mafunso onse akuluaakulu a moyo. Ndipo chuma ichi ndikufuna kukupatsani inuyo, koma pano pali khomo lakupanga chiganizo- kugonjera.”

Kugonjera ndi **njira** imene madalitso akulu ndi abwino a Mulungu amatsikira.

Tsopano, mudzazindikira ndayika chidziwitso cha uzimu pa chipepala cha zolembamo chifukwa pomwe mukungoyankhula ngati ndakhala ndukuyakhula zokhudza kudzipereka kwathunthu ndi ngati mukuyamba kuganiza za izo, pali magalasi amene tikuwonera.

Mukudziwa, nkhani ya John ndi Sheilla inalidi yabwino. Ndipo mukuganizira za $100 miliyoni imene sheilla ali nayo ndi kuganizira za $30 kapena $40 miliyoni imene John anapeza kuchokera ku malonda chifukwa anali ndi chidziwitso cha mkati ndipo onse anali ndi kulimbikira mtima kowomba mfuti ndi kupanga mgwirizano ogula.

Mongodutsamo, ndisanapitilize, kodi muchipinda muno mulibe chifundo? Kodi pali wina aliyense amene akumumvera chisoni Sheilla? Anasiyana ndi galimoto yake ya volkswagon jetta, ndi chili chonse chojambula chake chili chonse chimene anagula kale zaka zambuyomo, simukuganiza kuti iye - mmalipiro ake ochepa a uphunzitsi—anali wolumikizidwa mmaganizo ake ndi zimenezo?

Ndipo John, ngati wakhala akupita ku malonda a katundu ngati ameneyu, pomwe anagulitsa chilichonse chimene anali nacho, kodi mukuganiza kuti pali zinthu zina zakale zimene zinachokera ku malonda ena zimene zinali za phindu kwambiri kwa iye? Mkazi wake aluza nyumba yake? Ndinu gulu la anthu owuma mtima choncho mukunenadi kuti mukuganiza kuti $30 kapena $40 miliyoni inali yaphindu kuchitira zimenezo? Indedi mukutero.

Tsopano, Yesu ananena mafanizo awiri awa kuti afike mudziko lawo munjira imene akanapezera magalasi ena atsopano, chifukwa pomwe mukuyakhula kwa anthu amene akufuna kutsatira Mulungu mokhudza kudzipereka kwathunthu, ndi “Chabwino, ndikudziwa abusa amene anayenera kudzipereka kwathunthu ndipo mwina mwake otumikira kunja kwa dziko lawo ndipo pali nthawi

zonse mayi wokalamba wazaka 98 amene amapempheradi ngati maola 37 patsiku koma pali maola 24 okha pa tsiku.

Ndipo tikudziwa kuti ndi odzipereka kwathunthu, koma ndikutanthauza, ndife Akhristu a achizolowezi ndipo icho chikuwopseza ndipo ndikufunitsitsa kukonda Mulungu. Ndine wokondwa ndikupita kumwamba, ndine wosangalala Yesu anandikhululukira machimo anga ndipo ndikufuna kukhala munthu wabwino.

Moonadi, ndikuganiza kuti ndine munthu wabwinoko kuposera anthu ambiri. Koma kudzipereka kwathunthu kukumveka moopsa. Mulungu ali ndi choyankhula pa nthawi yanga, ndalama zanga, tsogolo langa, banja langa-ah.

Choncho, chimene ambiri mwa ife timachita ndi chakuti timaona magalasi a kudzipereka kwathunthu moyipa. Moonadi chidziwitso chimene ndinayika mu zolemba mwanu… tikuwona kudzipereka kwanu kwathunthu monga **chopereka nsembe**. Timaona ngati **kudzikana**. Timawona ngati **wolemekezeka**. Timaganiza kuti anthu amene ndiodzipereka kwathunthu ngati **ofera chikhulupiriro.** Kodi munayamba mwakumananako ndi wina wake amene anati, “Ndinasiya zonse chifukwa cha Yesu?” Ndinakumanako ndi ena monga amenewo ndipo sindinakonde kukhala pakati pawo kwa nthawi yawo chifukwa anakana zonse ndipo penapake amenewo amaganiza kuti ali bwino kuposera inu ndi ine.

Pano pali chimene ndikufuna kukuuzani pomwe Yesu anaphunzitsa zokhudza kugonjera kapena kudzipereka kwathunthu, ndi njira imene mungapezere chabwino kwambiri cha moyo wanu kuchokera kwa Mulungu. Koma anati ndi chimwemwe. Cholinga chake ndi chabwino ndi chanzeru ndi zomveka wochenjera. Sikuti kwambiri ndi kukana monga ngatinso kuunikanso. Kodi $95000 ndi yaphindu lofanana ndi $30 mpaka $40 miliyoni? Ichi sisayansi yapangira ndege ya roketi. Tsopano, ngati tingachiyanga’ane choncho ndi chosavuta. Koma mukayang’ana chuma chimene Mulungu ali nacho, zimayamba kuvuta chifukwa simungathe kuchiwona.

Tsopano, Yesu anagawa chimenecho ndi kupanga mafanizo awiriwo kuti afikire dziko lapansi. Kwa inu amene mwina mungakhale ndi lamya ya mmanja kapena komputa ya mmanja ndipo mwaganiza kuti izi zikumveka monga bukhu losangalatsa ndipo mwafufuza kale pa Google “Chiwopsezo, Chifukwa, ndi dongosolo lopanga chiganizo” musadikilire kuti Google kuti ibwere. Monga momwe Yesu anapanga mafanizo awiri kuthandiza anthu mdziko lawo kumvetsa chimene chikuchitika. Ndinamasuka kupanga nkhani zofunikira kuganizira ziwirizo chonde musadzimve ngati mwaperekedwa.

Ndikanabwera pano ndi kunena kuti “kudzipereka kwathunthu, kugonjera ndi njira imene madalitso akulu ndi abwino a Mulungu amatsikira. Tsopano, kodi inu ndi odzipereka kwathunthu kapena ayi? Kodi muyima kapena ayi? Kodi mupitiliza ndi pulogilamuyi?”

Zonse zodziyikira kumbuyo zanu zikhala chiyani? Uh ... Uh. Uh... Ndipo mukhala kuti mwaphonyeratu mfundo yake. Ndinali mwa iwo amene wogwedezeka muchipembezo amene ndinaganiza kuti ndili bwino kuposa ena chifukwa ndinali wodzipereka. Ndinaphonyeratu mfundo, sindinamvetse chisomo cha Mulungu.

Koma inu nonse amene mwakhala ngati mukuganiza patsogolo... Pano pali chinthu chimodzi chokha chimene munaganiza kuti Sheila ndi John - ndikanakonda ndikanakhala ngati iwo. Zoona? Ndikulakalaka ndikanakhala iwo. Kodi mukudziwa? Pali wina wake anganene, “Oh Sheila ndi John anali wolemekeza, anali ofera chikhulupiriro, analuza Jetta zoona? Anapereka nsembe yayikulu. Kodi cholunjika chanu chili kuti? Cholunjika chanu chili ngati changa – nsembe. Ubwino wake, $30 mpaka $40 miliyoni, cholunjika chinali chimene anapeza.

Ndipo icho chinali mfundo ya Yesu. Umenewo ndiye uthenga wake kwa inu. Kumbukani, ichi ndi chokhudza mmene mungampatsire Mulungu chimene Akufuna kwambiri. Nthawi yathu yakhala pamodzi isanathe, tikhala ndi mphindi zodekha ndi zoyera zimene ndifotokoze ndendende mmene tingapatsire Mulungu chimene akufuna kwambiri koma zifuna sitepe ya chikhulupiriro yayikulu kudzipepereka kwathunthu ndi kugonjera. Ndipo chimene mungayambe kufunsa ndi mmene ndingagwire zinthu ndi maonekedwe anga ndi chimene ndikufuna molimbana ndi chimene iye angapereke. Kodi ndi chiti mwa izo chimene ndidzadalire?

Zikundikumbutsa za nthano imene ndinamva zaka zambiri zapitazo, ndipo inali nkhani ya tsikana wang’ono amene anapita kutchuthi ndi banja lake. Ndipo munali mmbali mwanyanja, ndipo anali mu imodzi ya nyumba zogonamo alendo zimene ukangotuluka pakhomo umapeza mchenga, ndipo mungathe kuyenda pagombe ndipo inali ndi phiri. Ndipo kumapeto kwa phiri kunali bwato lowedzera nsomba ndi munthu wokalamba.

Inali tawuni yaying’ono mu New England ndipo mtsikana wang’ono ameneyo, mwina wa zaka zisanu kapena zisanu ndi chimodzi, wokongola, wojijirika, mukudziwa ana amsinkhu umenewo mmene amachitira - amatha kupita kuphiri ndikubwerera ndikupitanso ndiye kumeneko kunali msodzi wansomba okalamba amene anali wodziwika mutawunimo ngati wovuta. Anali wongovuta. Anali wokalamba. Anali wowawidwa mtima. Anzake anali atamwalira kale. Anapilira mmoyo wovutika. Choncho anali atasiya kukumana ndi aliyense. Koma mukudziwa chinachake tsikana wang’ono wa zaka zapakati pa zisanu ndi zisanu ndi chimodzi Hii, Hii.

Chabwino, tsiku loyamba litatha, tsiku lachiwiri, tsiku lachitatu, tsiku lachinayi, mtima wake unayamba kumasuka. Ndipo palibe munthu amene anamusamala iye bwino. Ndipo tsiku lillonse amatola zikokombe ndi kumupatsa iye ndikukhala kumapeto kwa chitunda mapazi ake akulendewera. Posakhalitsa, nkhalamba ija inamupatsa mtsikana mbedza yake yowedzera nsomba.

Ndipo pa tsiku lawo lotchuti lachisanu ndi chiwiri, mgwirizano unapangika. Ndipo anazindikira “Palibe padziko pano amene amasamala za ine ndipo posachedwa ndidzafa.” Anali muzaka zake za ma 80. “Ndipo mtsikana uyu wang’ono akusamala za ine.”
Ndipo mosadziwika kwa ena, anali ndi chikwama chaching’ono kuchokera muzaka zake zausodzi wa nsomba ndipo anapeza zikokombe zingapo ndi ngale. Ndipo chimene anazindikira ndi tsikana wang’onoyu ndi chakuti amalendeweretsa mapazi ake, koma amagwiritsitsa mikanda yake ya mkhosi imene inali ya mtengo wotchipa imene mukanatha kuyipeza musitolo yotchipa. Mukudziwa inu, muli ku tchuthi, ana nthawi zonse amafuna zinthu zokongoletsera.

Ndipo anazindikira mmene anawukondera mkanda umenewo choncho anatenga ngale zake ndi kukhala nthawi yayikulu usiku wonse, kuboola mabowo mngalezo, anachotsa kachingwe kumbedza yake ndi kupanga mkanda wamkhosi. Anaganiza "Ndidzamupatsa mkanda wa ngale tsikana uyu wa zaka zisanu ndi chimodzi."

Ndiye choncho, tsiku linalo anabwera kudzatsazika ndipo ngolo ya galimoto inali itayima ndipo makolo anayima pamtunda wa mayadi 100 kuchokera pamene anali, "Chabwino, honey. Konzekani. Inde ungathe kupita kukatsanzika." Choncho anathamanga kukatsanzika ndipo nkhalamba inati, "Bwera kuno, Ndili ndi mphatso yako." Ndiye akuyenda kufika naye pafupi ndipo akhala ali pa mgwirizano ndipo akuti "Ndipatse mikanda yako ya pulasitiki ili mukhosi lako." Ndiye akutululutsa zanyezinyezi padzuwa ngale zenizeni.

Tsopano vuto limakhalapo ukakhala wa zaka zisanu kapena zisanu ndi chimodzi ndi lakuti ndiwe wosakhwima___ sudziwa phindu la chinthu mmene chilili. Zimene umadziwa ndi zimene umamasukanazo. Chimene umadziwa ndi chimene chikumveka chabwino ndipo choncho, anatenga sitepe ina ndi kunena, pano ndili ndi izi. Izi ndi ngale zenizeni. Tsopano, chotsani izo ndikuvekeni. Tsopano, chotsani izo kuti ndikuvekeni izi." Ndipo tsikana wang'ono anabwerera mbuyo, analanda mkanda wake wa pulasitiki ndi kuthamanga mtunda wa mayadi 100, kudumphira mu galimoto ndi kunena kuti, "Ndikufuna dzipita. Abambo awo akufuna kutenga ngale zanga."

Ndikufuna ndikuuzeni mwa Akhristu asanu ndi anayi, muli akhristu asanu ndi atatu amene mowonadi amakonda Mulungu, amakakamila ngale za pulasitiki ndipo sakulandira china chili chonse pafupi zochitika mmoyo wawo, ubale wawo, kapena kukhudzika kwa muyaya, ku chimene Mulungu wasankha ndi kupangidwira kwa iwo kuti akhale nacho chifukwa pomwe iye akuti, "Ndipatseni inu. Mundiike Ine woyambirira pa nthawi yanu, Mundiyike Ine woyambirira mu tsogolo lanu. Mundiyike Ine woyambirira mu ziganizo zanu. Mundiyike Ine oyambirira mu banja lanu, mundiike Ine woyambirira mu ntchito yanu, mundiike Ine woyambirira mu ndalama zanu… Ndikufuna inu kuti mundidalire kwathunthu chifukwa ndili ndi ngale, osati zinthu zopanda pake."

Ndipo ngati simukhulupirira kuti ndi wabwino, ngati sumukudziwa mtima wa Atate ndipo mmangokhala mozungulira kwambiri osamva chikumbumtima ndi chikhulupiriro chatheka kuti mukalowa kumwamba. Nidpo mukukamira ku chuma chosakhalitsa chopanda phindu cha pulasitiki. Koma mukakumana ndi anthu amene anapeza ngale wambiri, mumazindikira kuti zimangokulemererani kukutsitsirani pansi mmalo mozipatsa moyo. Kudzipereka kwathuntu, kugonjera ndi ngalande. Ndi njira imene madalitso akulu ndi abwino a Mulungu amatsikira.

Chimene ndikufuna kuchita ku nthawi yathu yatsalayi, ndikufuna kufotokoza makamaka mmene kudzpereka kwathunthu kumawonekera. Sitikutsogolera ku nthawi ina yake yakuganizira. Tikupita ku chiganizo cha nzeru kumene tikuyeza chiopsezo komanso Mfundo zathu kwa Mulungu m'mphindi zochepa. "Ndikupereka zonse kwa Inu. Ndingathe kusayinira cheke chopanda kanthu kwa Inu. Ndinganene kwa Inu kuchokera lero mpaka mtsogolo ndine wanu mu zonse. Ndikhoza kukhala wa mantha pang'ono koma ndili mu zonse."

Koma pofuna kuchita choncho, kodi chimenecho chimaoeneka bwani? Yankho lili mu Aroma 12:1 Patatha mitu 11 za chuma, za chimene Mulungu anachita, za mmene amakukonderani inu ndi za

ulamuliro wake, ubwino wake, chikhulupiriro chake, mphamvu zake, Mzimu wake wokhala mwa inu mphatso zake ndi dongosolo limene ali nalo kwa inu. Mu mutu 12 kuyankha kwanu ku zimenezo ndi "Chifukwa chake ndikupemphani inu, achimwene, achemwali, mamembala anzanga a banja limodzi" mtumwi Paulo akulemba "mwa zifundo za Mulungu kuti mupereke matupi anu nsembe ya moyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera."

Onani mapangidwe. Pali lamulo. Pali cholinga. Ndipo pali chifukwa. Ndikufuna inu mulembe bokosi mozungulira mawu akuti **kupereka**. Lembani bokosi pozunguliza **nsembe ya moyo.** Ndiye kenako, ikani kabokosi pozunguliza mawu **woyera**, ndiye kenako, ndikufuna mulembe mzere wokhotakhota pansi pa **Kupembedza kwanu koyenera.**

Lamulo ndi lakuti mupereke thup lanu kwa Mulungu. Izi sizamwambi. Ili ndi thupi lanu lanyama, maso anu, mutu wanu, manja anu. Zonse zomwe inu muli. Ndipo mawu akuti kupereka pano ali mu nthawi, mu chilankhulo cha chigreek ndi puncliar. Ndipo ichi chikutanthauza kuti "tsiku lina pa nthawi ina." Ndimeyi sikulongosola mmene mungakhululukidwire machimo anu. Ndimeyi sikulongosola chimene akutanthuza kukhala m'mbanja la Mulungu. Chipulumutso chikupezkea kumapeto kwa mutu wachitatu, wachinayi ndi mkati mwa mutu wachisanu, ntchito ya Khristu mwa chisomo. Mumalandira mphatso mwaulere mwachisomo. Mutu 12 ukunena, "Mmene Mkhristu wamba amatsatira Yesu mwakuyamika? Ndipo Mulungu akuti "Ichi ndi chimene ndikufuna. Ndikufuna tsiku lina pa nthawi ina, kunena kwa Ine. "Zonse zimene ine ndili zonse zimene ndili nazo ndi Zanu." Icho ndi chimene akutanthauza ndi kupereka.

Ndikuuza inu, kungochokera kuzokomana nazo zathu zikutiphunzitsa mu ndandanda uwu, makumi a zikwi za anthu ozungulira dziko samamvetsa njira imene madalitso akulu ndi abwino a Mulungu amatsikira. Mkhristu aliyense mwina mwake amagniza, "Ndinalandira Yesu, ndi Mpulumutsi wanga, ndi zoona zenizeni, ndimawerenga Baibulo pang'ono, moonadi ndikuyesetsa kwambiri kukhala Mkhristu wabwino koma sizikuyenda bwino."

Mphamvu ya moyo wa Mkhristu imalowera mu nthawi iyi yopereka. Kumbukirani mmene paipi yothirira mmunnda, pomwe muli ndi botolo lamadzi, imapindika? Mmene mumawongolera ndi pamene mukunena kuti, ndi njira, ndi Ngalande. Tsopano, kumafunikira chikhulupiriro. Kumafunikira kukhulupirira mu chuma chosaoneka chimene sungachione. Koma chili ndi mbiri, Mulungu wa moyo amene amayenda pano pa dziko lapansi ndi kufa mmalo mwanu ndi kuwukanso ndipo akukhala ku dzanja lamanja la Mulungu ndipo akunena kwa inu, "Pali chuma chosasimbika" amene mwachimwemwe akunena kwai nu, "Ndiloleni ndikupatseni chabwino kwambiri."

Zaka zanga ziwiri ndi theka zoyaba za Chikhristu, sindinadziwe. Ndinafika pa mulingo wakuti ndinalibe khalidwe chonsecho sindinawerengeko Baibulo. Ndinakhulupirira Yesu mu ntchuti cha chiilimwe chitatha chaka changa chomaliza sukulu ya Secondary. Nidnapita ku College ndipo zinanditengera miyezi itatu, inayi, isanu ndi isanu ndi umodzi kuti ndifike powerenga Baiblulo mwina mwake katatu kapena kanai pa Sabata.

Koma Mulungu analankhula kwa ine. Ndiye kenako ndinapita kosanthula Baibulo ndipo kumeneko kunali kupezeka kwa Mulungu ndi anthu a chikondi ndipo zinali zopatsa chidwi. Koma kenako, mukudziwa, ndnafunitsitsa kuti timu ya mpira ya basketball kuti indikonde ndipo kunali atsikana

onse awa. Choncho, inde kwa Mulungu, Chip, Mulungu, Chip ndipo mukudzwa usiku wa lachinayi kusanthula Baibulo, “Oho, ndinawona kupezeka kwa Mulungu.” Ndiye kenako usiku wa la chisanu ndi loweruka ndinapita kokayenda ndi anzanga mpaka mbandakucha. “Mulungu, pepani sindidzachitanso zimenezo.”

Ndinali ozunguza; zinthu zonsezi ndimazibisa mkati mwa moo wanga. Ndipo chimwemwe cha chipulumutso changa chinali kukwawa, chimakwawira pansi pamene ndinali kuyesetsa kuti ndidzidzutse mu uzimu, mukudziwa inu Mulungu mmene ine ndimalankhulira, ndimatsatira malamulo asnu ndi atatu ndi theka pa malamulo onse khumi. Kodi pamenepo sindikhoze 85 kwa 100? Ayi, chip.

Ndikukumbukira ndinapita ku msonkhano kumene zimene ndangokugawiranizi zinaphunzitsidwa. Unali moyo wa Abraham. Kunali anthu mwina 30 kapena 40 muchipinda chaching’ono cha msonkhano – ndipo wolankhula anatiyendetsa mu sukulu ya chikhulupiriro ya Mulungu. Ndipo anafika ku Genesis mutu 22 kumene Mulungu akunena kwa Abraham zokhudza mwna wake. “Tenga mwana wako wa mwamuna mwana wako yekhayo, amene umamukonda ndipo umutengere ku phiri ili ndi kumupereka nsembe kwa Ine.”

Ndipo Abraham ananyamuka mmawa. Anali atakhala ndi Mulungu nthawi yayitali – ali ndi zaka 100 tsopano. Ndipo tinaphunzira kuti anaphunzira kuti pomwe Mulungu akunena china chake, mungathe kumudalira. Ngakhale chinaoneka kuti ndizosamveka, zopanda nzeru, anapita anatenga mpeni ndipo anali wokonzeka kutsika, ndipo Mulungu anati, “Siya, tsopano ndadziwa kuti ndiwe okhulupirika kwa Ine chifukwa unapereka mwana wako, mwana wako yekhayo amene umamukonda.”

Ndiye isanafike nthawi imeneyi, Mulungu anali atapanga malonjezo ena kwa Abraham okhudza zidzikulu zake ndi zatsogolo lake zimene zinali zazikulu kwambiri. Itatha nthawi imeneyi yogonjera mu mutu 22 Mulungu akukulitsa, kukulitsa, kukulitsa nd kunena, “Ayi, Abraham ichi ndi chimene ndichite tsopano, chifukwa Abraham, sindinafune mnyamata wako, sindinafune nsembe chimene ndinafuna ndi mtima wako.” Ndipo mnyamata ameneyo anakhala fano. Ndipo nthawi iliyonse ngati pali chinthu china pamaso pa ubale wanu ndi Mulungu ndipo muli ndi fano, mudzaphwanya fano, apo ayi, fano lidzaphwanya inu ndipo ichi chidzawononga ubale wanu ndi Mulungu.

Ndipo icho ndiye mikanda. Izo ndi ngale za pulastiki. Ndipo pakhoza kukhala ntchito ndipo pakhoza kukhala banja ungather ukhala ubale, zingathe kukhala ndalalma, zingathe kukhala kudzimva, zingathe kukhala thupi lanu. Tonse ife tili ndi a Isake. “Pokhapokha ngati mbeu ya tiligu yagwa mu nthaka ndi kufa, imakhala payokha. Koma ngati yafa, imabereka zipatso.” Ameneyo ndi Yesu.

Kotero ndikufuna kuchotsa mafano anga – kwa ine, inali basketball ndi chibwenzi changa – zinali zimenezi. “Mulungu, ndidzachita chilichonse chimene Inu mukufuna. Koma muskhudze basketball ndipo musakhudze chibwenzi changa.” Ndipo kumbuyo kwa chipindacho cha anthu 30 kapena 40, ndikukumbukira ndinapanga chiganizo chosintha moyo wanga, kupatula kulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanga.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

Ndi mantha ndi kunjenjemera ndinagwada pamowondo anga ndi kunena kuti, “Mulungu ndili ndi mantha akulu chifukwa Inu mudzandipanga kukhala wosakwatira moyo wanga wonse kapena kuposera apa, ndidzakwatira munthu wosakongola.” Chabwino ndikungokuwuzani mmene zinalili? Ndinali ndi zaka 20. Ndinadziwa chiyani?

Ndiye kenako ndinati, “Ndipo Mulungu ndakhala ndikusewera basketball moyo wanga wonse ndi pomwe ndatenga mpira mkati mopumira, ndimakonda masewera awa ndi … koma Ndinu Mulungu. Ndikuthanthauza, chonde musandichotsere chimenecho, koma ndi fano. Ndipo ndikufuna Inu mudziwe kuti ndili mu zonse. Sindikudziwa kuti zimawoneka bwanji, koma ndidzakhala moyo ndipo ndi wotsimikizika kuti ndidzawononganso mtsogolo, koma ndidzakhala moyo munjira yanu kupita mtsogolo. Chilichonse chimene Mawu Anu akunena. Ngati akunena, ndipanga chiganizo choyamba, mwina ndingawononge koma ndidzabwereranso pa nthawi iyi. Ndikupereka mtima wanga, zolinga zanga, tsogolo langa, ndalama zanga, maloto anga. Ndikufuna kukhala moyo mu njira Yanu.” Ichi ndi chimene chikutanthauza kupereka thupi lanu.

Ndiye kenako, zindikirani sichakumva mmaganizo pakamodzi. Kodi bokosi linali ndi chiyani? Ndi nsembe yamoyo. Koma mumapereka thupi lanu monga nsembe yamoyo, choncho nsembe yamoyo ili ngati banja. Mu 1978, ndinanena kwa Theresa, ndikudzipereka kwa iwe, osati kwa wina aliyense koma iwe Wekha. “Ndipo iye anati, ndikudzipereka kwa iwe.” Ndipo tinati tidzachita izi pamodzi mpaka kalekale, osatengera chilichonse.

Koma ndinayenera kuchita izi pafupifupi tsiku lirilonse. Ndipo panali nthawi zina zimene tinasowekera uphungu wa banja. Tinali ndi nyengo zina zokhoma ndi ana athu ena ndipo takhala ndi zinthu zokhudza umoyo wathanzi ndipo tinapezekako ndi matenda a Khansa. Takhala ndi mavuto a mitundumitundu koma chifukwa tinati, “Tikudzipereka kwa wina ndi mnzake osatengera chilichonse… Kunali kudzipereka kumene kwatisunga pamodzi.

Ndipo chakhala njira ya madalitso akulu ndi abwino ochokera kwa Mulungu. Tsopano zatha zaka 33 zapitazo zakuti sinangokwatira kokha ayi, ndili ndi mkazi wabwino, ndili ndi mkazi wokhulupirika, ndili mnzanga amene sindinakhale nayepo. Ndili ndi ubale umene sindinauwonepo ndikukula mbanja mwathu. Ndinali ndisanalotepo mmoyo wanga kuti ndidzakhala nazo. Kodi zakhala zophweka? Ayi, koma zokhala zabwino kwambiri.

Ndiye kenako Mulungu… Akuchita chiyani? Mulungu ndi woseketsa, ndinasiya basketball koma zinanditengera nthawi. Minyewa yanga yokungana inatha ndipo chaka chimenecho ndinaluza zambiri. Kenako ndinapweteka, kenako anasintha mphunzitsi, ndi mapeto ake kunali “Chabwino, ndili bwino.” Pamapeto a chaka changa chomaliza, “Ndidzachita mu njira yanu, Mulungu.” Kudzipereka.

Ndipo Mulungu anatembenuka nditamaliza maphunziro anga ndinasewera basketball mmaiko onse a ku South America. Ndipo ndinali pang’ono NAIA. Mukudziwa, iyi inali gulu la Gawo Lachitatu sukulu yaying’ono. Ndiye kenako, ndinagonjera, Mulungu anandiika mu timu yachiwiri ndipo ndinasewera molimbana ndi matimu a ku Olympic a ku South America onse ndipo kenako ndi timu ya ku Australia mu Orient monse.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

Onani nkkhani siyakuti akufuna kukutengerani china chake chabwino kwambiri. Nkhani ndi yakuti chilichonse chabwnio kwambiri chimene chimakhkala pakati pa inu ndi Iye ndi fano. Ndipo chidzawononga ubale wanu ndi Iye. Mongokuwuzani, chidzawononga ubale wanu ndi fano.

Choncho ndi nsembe yamoyo, koma kenako ndi moyo wotsitsimutsa ndi kukhala tsiku lirilonse. Ndi woyera awa ndi mawu omaliza. Ndi **woyera.**

Simungathe kubwera kuno ndipo osathana kaye ndi chinthu chanu. Pali ena mwa inu amene mwakhala pa nthawi ino mukuganiza, "Ngati ndingapereke ubale wanga ndi mnyamata kapena mtsikana uyu wowonongeka amene ndikudziwa kuti sichifuniro cha Mulungu ndidzamva kuwawa ndiponso ndimamukonda…" Mulungu adzanena, "Mukudziwa kuti sizolondola," Enanu mwazindikira kuti kukhala ndi mwamuna kapena mkazi musanakwatirane sichisankho cha kugonjera kwanu. Kwa ena mukunena kuti, "Zofunikira zanga ndi zambiri, ndimagwira ntchito molimbika kapena chuma changa chasokonekera."

Onani, ndi choyera. Nkhosa yopanda chilema. Akutero. "Mubwere mmene mulili." Koma pali kudzikhuthula uku konena, "Mulungu, sindikusewera masewero, ndikhala moyo mnjira Yanu. Ndiye kenako ndibweresa zanga zonse." Ndi ichi sizinthu zabwino zokha, koma mubwere munene kuti, "Ndikubweretsa mantha akukanidwa, ndikubweretsa mantha a tsogolo langa. Ndikubweretsa mantha a chimene mungachite. Ndikhulupirira kuti Inu ndi Mulungu wabwino."

Moonanso tazindikirani chilimbikitso. Chilimbikitso sichakuti "mukhale ndi ndondomeko." Ndi chifundo cha Mulungu. Akuyang'ananso mitu 11 ya mbuyomo ya Aroma ndiponso akuti, "Mulungu akupempha chilichose cha inu. Koma wachita chiyani? Anakukondani. Anakukhululukirani. Analipira machimo anu. Anapangitsa Mzimu kubwera mu thupi lanu. Anakuchotsani ku ufumu wa kumdima ndi kukuyikani mu ufumu wa kuwala. Anakutengani kukhala mwana. Ali ndi cholinga ndi moyo wanu. Akukulengerani malo anu tsopano lino. Anapereka moyo wake."
Akunena kuti, "Kodi simungandidalire?" Ichi chili ngati kuti wna wake wakupatsani mamiliyoni a ndalama ndipo akubwera kwa inu kudzati, " Hey! Kodi mungathe kundibwereka &20? Akunena kuti, "Sindikudziwa ngati mungandibwezere!" Ndipo inu mukuti, "Mukutanthauza chiyani?" Simukudziwa ngati ndingabwezere?" Ndinakupatsani miliyoni ya ndalama," Eya, chabwino sindikudziwa."

Kodi mwayamba kumva nzeru za Ufumu? Simungamve bwanji – kwa Mulungu amene wawonetsa chikondi chenicheni, pomwe inu munali mdani Wake ndipo ine ndinali mdani Wake – anapereka moyo wake …Sitingakhulupirire bwanji kuti Iye ndi wabwino, ndi wachifundo kuti ndi wokoma mtima? Ichi sichikungokhala pa ndondomeko. Khalani Mkhristu wapamwamba kwambiri. Ichi ndikulolera Atate Anu akukondeni. Tiyeni tichotse zotchinga.

Ndipo chifukwa chomaliza ndi kupembedza kwanu kwa uzimu. Mmau ena, chimene Mulungu akufunitsitsa. Tinayamba ndi funso limene linatitsogolera ku chiganizo. Funso ndi ili, Kodi mungamupatse bwanji Mulungu chimene Iye akufuna kwambiri? Kodi mwakonzekera ichi? Ndi chophweka Mulungu akufuna inu, chilichonse chanu, chilichonse chokhudza inu.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

Mungathe kuwerenga Baibulo, mungathe kupemphera, mungathe kubwera ku tchalitchi, mungathe kupereka ndalama, mungathe kuyenda ulendo wokutumikira kunja, mungathe kuyesa kukhala wokhalidwe labwino, mungathe kuchita zinthu zina zonsel…Panali gulu mu Chipangano Chatsopano limene linachita zonsezo ndi kuposeranso pamenepo, ndipo Yesu analankhula zinthu zowopsa kwambiri zimene sanalankhuleponso kuchokera mkamwa mwake zokhudza anthu a chipembedzo amenewo chifukwa chakuti mitima yawo sinali yake. Amawawongolera ndipo anagwiritsa ntchito chipembedzo chawo, ndipo anaganiza kuti iwo ali bwino kuposera ena. Sanali wofewa. Sanali wosweka. Sanali wokonda.

Titatsala tokha ndife anthu amene tingadzipangire malire kapena chifanizo cha mmene ife tilili bwino ndi Mulungu chifukwa tikuchita ichi ichi ichi ndi ichi pamene tikupindula ndi kuwongolera. Ndipo kuwongolera kwanu kuli konse komaonekera ndi kumene ndalama zanu zimapita. Kumene nthawi yanu imapita, kumene mphamvu zanu zimapita ndi zimene mumalota. Ndipo pamene ali ndi mtima wanu, mmadera emenewo, zinthu izi zimasandulika.
Ndiye kenako mumazindikira chifukwa chimene muli pano. Mumazindikira cholinga, mumazindiira kuti mmoyo muli zina zofunikira kwambiri kuposa kuyika zolinga ndi kuzikwaniritsa izo. Mumazindikira chuma chapano ndi lonjezo la muyaya.

Akufuna Inu.

Ndinafuna ndingokupatsani zinthu ziwiri zimene zakhala zothandiza kwambiri kwa ine. Chimodzi ndi cheke chopanda kanthu. Ndinayika ichi mu zolemba zanu, Cheke ichi chopanda kanthu, kwa ambiri a inu uku kudzakhala kuyamba kugonjera kwenikweni….

Ndipo ndikufuna kukuwuzani, Chonde musamvere zakuti chilichonse chidzakhala chophweka ndi chokondweretsa ndi chachikulu. Moonanso, ambiri mwa inu mudzayesedwa. Abraham sanatenge mpeni wa labala pokwera. Zikhoza kupitirira kuwawa zisanakhale bwino koma Mzimu Woyera adzanena, “Chabwino, kodi zikuyenda bwanji mnjira ya inu eni?”

Ndipo lero, lipirani ku dongosolo la Yesu Khristu. Ndipo pali tsiku, mulemba tsiku la lero ndiye kenako musayinira dzina lanu. Ndipo mudzamva mantha mkati mwa mtima wanu. Koma adzakhala sitepe ya chikhulupiriro ndipo mudzanena, “Ndilmo ndense, Mulungu. Mungathe kutengamo ndalama. Mungathe kutenga tsogolo langa. Mungathe kutengamo maubale anga. Mungathe kutengamo chuma changa. Mungathe kutengamo ntchito yanga. Mungathe kutengamo Kumalo kumene ndimakhala. Ndidzachita chilichonse chimene mungandiuze, kuti ndichite. Ndikhulupirira kuti ndi abwino ndi okoma mtima. Ndipo makamaka ndikhulupirira kuti mungathe kutola chimene chili chabwino kwa ine kuposera mmene ine mwini wake ndingatolere.”

Kodi mukuona kuti mmadzitukumula bwanu mukamanena kwa Mulungu, “Eeh, ndikufuna chikhululukiro chanu ndi chipulumutso chanu, koma ndidzayendetsa moyo wanga mnjira yosamala, tandioneni ine.”

Choncho ndikufuna inu muganize za chiopsezo, chifukwa ndi ndondomeko yakupanga chiganizo.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

Ndinawerenga gawo la pemphero laling'ono la mayi wotchedwa Ruth Myers. Ndinayedzeka mmbuyo- mukhoza kutseka maso anu - pomwe mwaganizira za zimene zikutanthauza kwa inu pamene mwasayinira za pemphero limene liyende chonchi.

"Ambuye, ndine wanu. Posatengera kuti mtengo wake ndi otani, chifuniro chanu chichitike mmoyo mwanga. Ndazindikira kuti sindili pa dziko lapansi kuchita zinthu zanga kapena kufuna kudzikwaniritsa ndekha kapena kusinkhasinkha ulemerero wanga. Sindili pano kusangalatsa zokhumba zanga kapena kukondweretsa anthu, kapena kutchuka kapena kutsimikizira kuti ndine wina wake wofunikira kwambiri kapena kudzikweza ndekha. Ndiponso sindili pano kukhala wofunikira ndi wopambana mu muyeso wa umunthu. Ndili pano padziko lapansi kukusangalatsani Inu. Ndiye kotero tsopano ndikupereka ine mwini wake kwa Inu, pakuti Inu ndiwoyenera. Zonse zimene ine ndili kapena ndikuyembekeza kukhala ndikuzipereka kwa Inu. Ndine Wanu pachilengedwe ndipo ndine wanu pa mtengo Wanu pa mtanda pamene munandilipiria machimo anga."

"Ndipo kotero tsopano, ndikupereka kwa inu thupi langa ndi zigawo zake zonse. Zonse za mkati mwanga. Ndikukupatsani maganizo anga, zakumva mmalingaliro a moyo wanga, chifuniro change, okondedwa anga, banja langa kapena chiyembekezo cha banja. Panopa ndikukupatsani kuthekera kwanga ndi zofooka zanga, thanzi langa ndi udindo wanga - kaya wapamwamba kapena wapansi. Ndikukupatsani katundu wanga, kale langa, tsopano langa ndi tsogolo langa. Ndipo ndikudzipereka kwa inu pomwe mukufuna inu kundibweretsa kwathu kuti ndikakhale ndinu. Ndili pano kukondani inu ndi kumvera inu ndi kulemekeza inu."

Kodi ndinu wokonzeka kutenga sitepe imeneyi? Chidzakhala chisankho chabwino zedi chimene mungapange.

Ndipo ena mwa inu muli osungulumwa pang'ono, ngati mumasewero kwambiri masewera a video, kuwonera kwambiri TV, muyenera kupita kwambiri kukawonera kanema, mumapezeka nokha kukagula zinthu kapena kudya kwambiri mukudziwa kuti zimenezo ndi chiyani….. izi ndi zizindikiro za moyo wosungulumwa icho ndi chizindikiro chodzipatsa nokha makhwala ndi mikanda ya ngale ya pulasitiki.

Ndinali ndi zolimbana nazo pakukula kwanga ndisanakhale Mkhristu. Ndimakonda kuyenda malo ovuta. Ndimakonda chisangalalo. Ndimakonda zinthu zovuta. Ndipo kotero wina wake anandidziwitsa ku makadi, choncho ndinasewera makadi mausiku lachisanu, ndipo ndinapanga njuga. Ndiye kenako ndinatengeka ndi othamangitsa a kavalo (hatchi) kotero kuti muchaka changa chomaliza cha sekondale sukulu, mmausiku a lachiwiri ndi lachisanu, ndi masewera pa kavalo. Sindikudziwa kuti ndingakuuzeni bwanji mmene chisangalalo changa chinalili tsiku loyamba kubetcha kwanga ndita betcha ndalama ziwiri koyamba ndi ku wina zochulukitsa $103. Ndinaganiza kuti imeneyo inali njira yophweka kwambiri yopangira ndalama.

Ndiye kotero zinaluunjika muulendo wovuta umene ndinapezeka chaka ndi theka kenako kumene ndinapezeka ndili mu chimbudzi cha anyamata, ndinayika mapazi anga pa mtondo kuti asandione. Ndiye pamene oyang'anira atatu a timu ya mpira wa miyendo amene ndinali nawo ngongole ija ndalama za mazana angapo amabwera kudzalonjerera ngongole yawo munjira yosayenera ya

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge

thupi langa. Ndinapanga chiganizo chosiya njuga. Sindinali Mkhristu. Panalibe cha uzimu chilichonse chinali ngati. “izi ndi zachabe ndipo ndi vuto.”

Koma ndikuwuzeni, ndikayatsa TV ndipo mawu akuti World Poker “Texas Hold Em” awonekera. Ndimangotseka. Ndiye pano pali chimene ndimakonda, chifukwa pali lamulo/fundo lalikulu zedi. Mukudziwa. Inu linali tebulo lotsiriza. Amakhala ndi milu iyi yonse ya ma miliyoni ya ndalama. Mpikisanowo unali wa ndalama zokwana $14.7 miliyoni. Makadi ogwiritsa apansi awiri… Kudziyika pachiwopsezo kumeneko- hmmm, awa ndi makadi abwino. Chifukwa … kuwunikanso chilichonse chimene ndakhala ndikuona munthuyi akuchita. Kuchitapo kanthui … chikhulupiriro…. Mungathe mwina mwake kumaliza pamodzi ndi ine, sichoncho? Ndalowa chonse.
.
Ndiye kenako, chimachitika ndi chiyani? Magetsi amachitika. Sewero limasinthiratu. kenako amayima. Amayamba kuyendayenda mozungulira. Chifukwa chiyani? Chifukwa chake nachi. Chifukwa china chake chichitika. Palibe mphotho mpakana mufike pa mulingo (mfundo) umene mudzanene, “Ndalowa chonse” mwina akhoza kutenga chibangiri ndi maliyoni ochulukitsa a ndalama kapena adzaluza.

Ndipo ndikufuna kukuwuzani kuti Mulungu wa dziko lonse lapansi wakubweretsani inu muchipinda china pa tsiku lalero kuti inu munene kwa iye. “Ndalowa chonse.” Ndipo mukatero, mudzayamba kumva mphamvu ndi kusangalala ndi kubetchera ndi cholinga zomwe simunazidziweko chifukwa monga achitira mu “Texas Hold Em,” masewerowa safika pokoma mpaka mutalowano.

Ndipo choyang’anitsitsa chachisoni changa ndi chakuti Akhristu ambiri amene ndimawadziwa akungoyesetsa kukhala anthu abwino, kuti akhaleko bwino mmayendedwe a banja lawo. Kuyesetsa kupeza mmene angakwanitsire zosowekera zonse za pa moyo, mwaulemu pang’ono kuposera anthu ena onse, kuwerenga Baibulo lawo tsopano ndiye kenako kubwera ku tchalitchi ndi kudzayika mchere pang’ono pa kulakwa kwa moyo wanu. Ndipo Atate wanu wakumwamba, ndikuganiza ali ndi misozi mmaso Mwake, akunena “Kodi ndi chifukwa chiyani simukufuna kulawa chumacho?”

Popanda chikhulupiriro, ndikosatheka kusangalatsa Mulungu. Koma kwa iwo amene abwera, tiyeni tikhulupirire kuti iye ndiwopereka mphotho kwa iwo amene amamufunitsitsa Iye.

Copyright © 2023 Zolembedwa ndi Chip Ingram and Living in the Edge